PHUNZIRO LA 17

1. Kodi chinachitika ndi chiyani ana achimuna a mu mtundu wa Seti atayamba kukwatira ana achikazi a mu mtundu wa Kayini?
-Anthu ambiri samkafuna kumumvera Mulungu.
-Anthu ambiri amkamumvera Satana yekha.

2. Mulungu analankhula kuti adzilankhulana ndi anthu kwa zaka 120 zokha, kodi ngati anthu anakapitirizabe kutsatira njira zawo, Mulungu anakachita chiyani kwa iwowo?
-Mulungu anakaŵalanga ndi imfa.

3. Kodi Mulungu amkalankhula bwanji kwa anthu?
-Mulungu Mzimu Woyera amkalankhula m'maganizo mwawo.

4. Kodi Mulungu Mzimu Woyera amkalankhula chiyani kwa anthu?
-Mulungu Mzimu Woyera ankawawuza anthu kuti adzimvera kwa Mulungu osakhala kwa Satana.
-Mulungu Mzimu Woyera ankawawuzanso anthu kuti adzitsatira njira ya Mulungu yekha asakhala njira yawo.

5. Kodi Satana nayenso amalankhula ndi anthu kupitira m'maganizo awo?
-Inde.

6. Kodi Satana amawawuza chiyani anthu?
-Satana amawawuza anthu kuti asamamumvere Mulungu.

7. Kodi anthu amkachita chiyani?
-Anali ozikonda ndiponso awumbombo.
-Anali oyipa ndiponso achisokonezo.
-Samkayifuna njira ya Mulungu.

-Amkangofuna njira yawo yokha.

8. Kodi anthu a masiku ano ndi ofanana ndi anthu a m'masiku a Nowa?
-Inde.

9. Kodi Mulungu amkaŵawona machimo awowo?
-Inde.

10. Chifukwa chakuti dziko la pasi linadzadza ndi machimo a anthu, kodi Mulungu anaganiza zochita chiyani?
- Mulungu anaganiza zowononga za moyo zonse za pa dziko la pansi.

11. Chifukwa chiyani Mulungu anaganiza zomupulumutsa Nowa?
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti anabadwira mu uchimo.
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti wamuchimwira Mulungu.
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye ku machimo ake.

12. Kodi Nowa anamulamula chiyani Nowa?
-Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo.

13. Kodi Mulungu amkafuna kuti Nowa apange chombo mu njira yake ya Nowayo?
-Iyayi.

14 . Kodi Mulungu amkafuna kuti Nowa apange bwanji



ndi ine pamodzi ndi mtundu onse umene ukudza, ndiponso cholengedwa chilichonse chimene chili ndi inu.
13-Ndikuyika utawaleza m'mitambo, ndipo udzakhala chizindikiro cha chipangano cha pakati pa Ine ndi dziko la pansi.

-Mulungu anamupatsa Nowa pamodzi ndi anthu onse chizindikiro.
-Chizindikirocho unali utawaleza.

-Kodi chizindikiro cha utawaleza chikutanthawuza chiyani?
-Chizindikiro cha utawaleza chimatanthawuza kuti Mulungu sadzawononganso dziko la pansi ndi chigumula cha madzi.

-Kodi Mulungu anasunga chipangano Chake?
-Inde.
-Mulungu sanama.

-Kuchokera mu nthaŵi ya Nowa mpaka tsopano, Mulungu sanawonongeko dziko la pansi ndi zonse za m'menemo ndi Chigumula cha madzi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 9:18-19

18-Ana a Nowa amene anatuluka mchombo muja anali Semu, Hamu, ndi Yafeti.
19-Ana a Nowa atatu amenewa ndiwo makolo a anthu onse a padziko la pansi.

-Ana amuna a Nowa anali Semu, Hamu, ndi Yafeti.
-Ana amuna a Nowa amenewa ndi makolo a anthu onse pa dziko la pansi.

-Iyayi.

-Magazi a nyama amamuphunzitsa Nowa kuti chilango cha tchimo ndi imfa yosatha.

-Kodi Mulungu anati chiyani kwa Nowa pamene Nowa ana-pereka msembe kwa Mulunguyo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 9:1-3

1-Mulungu anadalitsa Nowa ndi ana ake omwe, nati, "Mubale ana ambiri ndi kuchulukana, kuti mudzadze pa dziko lonse la pansi.
2-Za moyo zonse za pa dziko la pansi ndi mbalame zomwe, nyama zokwawa ndi zonse za mnyanja zidzakuwopani. Zonsezi ndaziyika kuti muzilamulire.
3-Tsopano mungathe kudya nyama zonse monga ndinakulorani kudya ndiwo za masamba. Ndakupatsani zonsezi kuti zikhale zakudya zanu.

-Mulungu anamudalitsa Nowa ndi banja lake.
-Mulungu anamupanga Nowa pamodzi ndi anthu onse kukhala olamulira nyama zonse, mbalame zonse, ndi msomba zonse.

-Mulungu anamupatsanso Nowa chizindikiro.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 9:8 ndi 11-13

8-Mulungu anamuwuza Nowa ndi ana ake kuti,
11-"Chipanganocho ndi ichi: "Ndikukulonjeza kuti sindidzawononganso za moyo zonse ndi chigumula. Ndithu, chigumula sichidzawononganso dziko la pasi."
12-Ndiponso Mulungu anati, "Nachi chizindikiro cha chipangano chamuyaya chimene ndikuchiyika pakati pa inu



chombo?
-Ngati m'mene anamulamulilira Mulungu.

15. Kodi Mulungu anamulamula Nowa kuti apange zombo zingati?
-Chombo chimodzi.

16. Kodi Mulungu anamulamula Nowa kuti apange makomo angati za chombocho?
-Khomo limodzi.

17. Ngakhale kuti Nowa anali asanayiwoneko mvura chiyambire, kodi iye amakhulupilira chiyani?
-Iye amkakhulupilira kuti Mulungu atumiza chigumula?

18. Kodi Nowa amkawawuza chiyani anthu pamene iye amkapanga chombo chija?
-Nowa amkawawuza anthu kuti adzimumvera ndiponso adzikhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi Mulungu amayiwala zimene walankhula kuti azichita?
-Iyayi.
-Kodi Mulungu amazichita zinthu zimene walankhula kuti azichita?
-Inde.

-Apa pali chitsanzo:

-Tsiku lina mwana wanu akuswa mphika wanu.
-Inu mwakwiya naye mwanayo.
-Kenako mukumuwuza mwanayo kuti mudzamupatsabe chilango.

-Kenako mukuliŵalira kumupatsa chilangocho.
-Kenakonso mukuliŵaliranso kuti mwana wanu anaswa

mphika wanu.

-Koma Mulungu sali ngati anthu.
-Anthu amayiwala, koma Mulungu sayiwala.

-Mulungu anamuwuza Adamu kuti adzafa akadzadya chipatso.
-Kodi Adamu anafa pamene anadya chipatso?
-Inde.

-Kodi Mulungu anayiwala zimene anamuwuza Adamu?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anachita zimene analankhula kuti adzazichita?
-Inde.
-Mulungu anamutulutsa Adamu ndi Hava m'munda mwa Edeni.

-Mulungu sali ngati anthu.

-Mulungu sadzayiwala kuchita zimene wanena kuti adzazichita.
-Mulungu nthaŵi zonse amachita zimene wanena kuti adzazichita.

-Mulungu sayiwala tchimo.
-Mulungu samayiwala kupereka chilango pa tchimo.

-Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse.
-Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.

-Mulungu anawadikira anthu kuti akhulupilire mwa Iye.

-Kodi Mulungu anawadikilira anthu nthaŵi yayitali bwanji



-Mulungu analankhula kuti adzamupulumutsa Nowa ndi banja lake.
-Nthaŵi zonse Mulungu amachita chimene wanena kuti adzachichita.

-Kodi Nowa anachita chiyani atatuluka mchombo muja?

Tiyeni tiŵerenge genesesi 8:20-22

20-Pamenepo Nowa anamanga guwa kumangira AMBUYE. Anatengako mtundu uliwonse wa nyama ndi mbalame zimene anthu amaperekera msembe, ndipo anazipha, napereka msembe yopsereza pa guwapo.
21-AMBUYE atamva fungo lokomalo, anati, "Sindidzatembeleranso dziko chifukwa cha zochita za anthu, chifukwa chakuti ndikudziwa kuti maganizo a munthu kuti ndi oyipa kuyambira ali mwana. Sindidzawononganso za moyo ngati m'mene ndachitiramu.
22-Nthaŵi zonse dziko la pansi m'mene lidzakhalire, padzakhala nyengo yobzala ndi nyengo yokolora. Padzakhala nyengo ya chisanu ndi nyengo yotentha, nyengo ya chilimwe ndi nyengo ya dzinja, ndipo usana ndi usiku zidzakhalapo kosalekeza.

-Chifukwa chakuti Nowa anali osangalala kwambiri chifukwa chakuti Mulungu anamupulumutsa iye, Nowa anapereka msembe kwa Mulungu.

-Chifukwa chiyani Mulungu analandira msembe ya Nowa?
-Chifukwa chakuti Nowa amakhulupilira mwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Nowa anasiya kutsatira njira yake ndikuyamba kutsatira njira ya Mulungu.

-Kodi magazi a nyamazo analipira tchimo la Nowa?

Masiku 150 atapita, madziwo anali atatsika ndithu,

4-ndipo pa tsiku la 17, mwezi wa chisano ndi chiŵiri, chombocho chinakayima pamwamba pa phiri la Ararati.

14-Pa tsiku la 27, mwezi wachiŵiri, dziko lonse la pansi linali litawuma kotheratu.

15-Mulungu anamuwuza Nowa kuti,

16- “Iwe ndi mkazi wako, ana ako pamodzi ndi akazi awo, tulukani mchombomo.

17-Tulutsa za moyo zonse zimene zili ndi iwezo, mbalame, nyama ndi zokwawa, kuti ziswane ndi kubalarika pa dziko lonse la pasi.”

18-Chomcho Nowa anatuluka mchombomo, iye ndi mkazi wake ndiponso ana ake ndi akazi awo.

19-Nyama zonse, zokwawa zonse, mbalame zonse, ndi zina zonse zoyenda pansi pano zinatuluka m’chombo-mo m’magulumagulu potsata mitundu yake.

-Mulungu anamukumbukira Nowa ndi banja lake pamene anali mchombo.
-Mulungu anayiletsa mvura, ndikuyitumiza mphepo kud-zawumitsa pa dziko la pansi.

-Anthu ena amanama kuti ziwanda zina ndi zimene zimalamulira mphepo ndi mvura.
-Ili ndi bodza.

-Mulungu yekha ndi amene analenga mphepo ndi mvura.
-Mulungu yekha ndiye wamkulu wa mphepo ndi mvura.

-Mulungu anamuteteza Nowa ndi banja lake m’chombo mu-ja.
-Mulungu anaziteteza nyama zonse zimene zinali m’chom-bo muja.
-Kodi pali amene anafa mchombo muja?
-Iyayi.



kuti iwowo akhulupilire mwa Iye?
-Zaka 120.

-Pamene Mulungu amkawadikilira anthu kuti akhulupilire mwa Iye, ukali Wake chifukwa cha machimo awo siwunachepe.

-Pamene Mulungu amkawadikilira anthu kuti akhulupilire mwa Iye, ukali Wake chifukwa cha machimo awo unapita mtsogolo.

-Ukali wa Mulungu pa tchimo umangopitilira mtsogolo.
-Ukali wa Mulungu pa tchimo umangopitabe mtsogolo mpa-ka pa nthaŵi imene imafika kuti Iye apereke chilango pa tchimolo.

-Kodi Mulungu anati chiyani kwa Nowa atatha kupanga chombo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 7:1-4

1-AMBUYE anamuwuza Nowa kuti, “Lowa mchombo pamodzi ndi banja lako. Ine ndawona kuti iwe ndi amene ukuchita zinthu zabwino mu m’bado uno pa dziko la pasi.

2-Tenga magulu asano ndi awiri a nyama, ziŵiriziŵiri, yayimuna ndi yayikazi, zimene amaperekera msembe, ndipo utengenso nyama ziŵiriziŵiri, yayimuna ndi yayikazi zimene samaperekera msembe.

3-Utengenso mbalame ziŵiriziŵiri za mtundu uli-wonse, magulu asano ndi aŵiri. Uchite zimenezo pofuna kuti mbalame ndi nyama za mitundu yonse zisungidwe ndi moyo, ndipo kuti zidzaswanenso pa dziko la pasi.

4-Pakangopita masiku asano ndi aŵiri, ndidzagwetsa mvura pa dziko la pasi kwa masiku makumi anayi, usana ndi usiku kuti zife za moyo zonse zimene ndinazilenga.

-Mulungu anamuwuza Nowa ndi banja lake kuti alowe mchombo.
-Mulungu anamuwuzanso Nowa kuti alowenso ndi nyama mchombo.

-Nthaŵi yinafika yakuti Mulungu aŵawononge anthu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amkafuna kwawononga anthu?

-Anthu samkakhulupilira kuti anali ochimwa.
-Anthu samkakhulupilira kuti tchimo lawo limkayenera chilango cha imfa yosatha.

-Anthu samkakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kwapulumutsa iwowo.
-Anthu samkakhulupilira mu lonjezo la Mulungu lomtumiza Mpulumutsi.

-Mulungu anadikilira zaka 120 kuti anthu atembenuke ku-chokera ku njira yawo kuti atsatire njira ya Mulungu.

-Koma anthu amkangofuna njira yawo yokha.

-Mulungu anadikilira zaka 120.
-Mulungu sanakadikiranso.
-Nthaŵi ya Mulungu yinafika yakuti apereke chilango kwa anthu.

-Lero, Mulungu ali chimodzimodzi.

-Mulungu akudikilira kuti anthu atembenuke kuchokera ku njila zawo ndi kutsata njira za Mulungu.



-Anthu ambiri masiku ano sakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene angaŵapulumutse.
-Anthu ambiri masiku ano sakhulupilira za chipangano cha Mulungu chotumiza Mpulumutsi.

-Anthu ambiri masiku ano amamumvera Satana osakhala Mulungu.
-Anthu ambiri masiku ano amaŵakonda machimo awo.

-Kodi inu muli ngati anthu ambiri a masiku ano, kapena mu-li ngati Nowa?

-Kodi pali amene anapulumutsidwa pa anthu amene anali kunja kwa chombo?
-Panalibe.

-Mulungu anati kuti anthu onse amene adzakhale kunja kwa achombo adzafa.
-Nthaŵi zonse Mulungu amachita zimene ŵalankhula kuti adzazichita.

-Kodi Mulungu anachita chiyani pamene anthu onse amene anali kunja kwa chombocho atafa?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 8:1-4 ndi 14-19

1-Tsopano Mulungu anamukumbukira Nowa pamodzi ndi nyama zonse za kuthengo ndi zoweta zimene zinali naye m'chombo muja. Anayilamura mphepo kuti iwombe pa dziko la pansi, pomwepo madzi anayamba kutsika.
2-Akasupe a madzi ambiri okhala pansi pa dziko pamodzi ndi zipata za ku thambo anazitseka. Ndiponso Mvura anayiletsa,
3-Ndipo madzi anayamba kutsika pang'onopang'ono.

-Mulungu atatha kutseka chitseko, anaŵapangitsa madzi onse amene anaŵayika kumwamba kuti agwe ngati mvura.
-Anthu anali asanayiwoneko mvura chiyambireni.
-Koma Mulungu anayipangitsa mvurayo kuti igwe masiku makumi anayi.

-Dziko lonse la pansi linavundikiridwa ndi madzi.
-Ngakhale mapiri atali atali kwambiri ndi mitengo yayitali-yitali kwambiri inamila ndi madzi.

-Mulungu akhoza kuchita china chilichonse.
-Palibe chimene sangachichite Mulungu.
-Mulungu yekha ndi amene ali ndi mphamvu zambiri.

-Kodi chinachitika ndi chiyani kwa anthu amene anali kunja kwa chombo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 7:21-23

21-Za moyo zonse zokhala pa dziko la pansi zinafa, monga mbalame, zoweta, nyama za kuthengo, mtindiri wa tizilombo tosiyanasiyana, ndi anthu onse.
22-Za moyo zonse za pa dziko la pansi zinafa.
23-AMBUYE anawononga za moyo zonse za pa dziko: anthu, nyama zokwawandi mbalame. Nowa yekha ndi amene anapulumuka ndi amene anali m'chombomo.

-Nyama zonse zimene zinali kunja kwa chombo zinafa.
-Anthu onse amene anali kunja kwa chombo anafa.

-Anthu ambiri masiku ano sakhulupilira kuti ndi ochimwa.
-Anthu ambiri masiku ano sakhulupilira kuti kuchimwa kwawo ndi koyenera kulandira chilango cha imfa yosatha.



-Tsiku lina, Mulungu sadzadikiliranso.
-Tsiku lina, Mulungu adzaŵalanga anthu onse.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 7:7-11

7-Nowa ndi mkazi wake ndi ana ake amuna ndi akazi awo analowa m'mchombo, kuthawa chigumulacho.
8-Nyama zazimuna ndi zazikazi zimene anthu amaperekera msembe ndi zimene samaperekera msembe, mbalame pamodzi ndi nyama zokwawa zomwe,
9-Nowa analowa nazo m'mchombo, ngati m'mene Mulungu analamulira.
10-Patangopita masiku asano ndi aŵiri, chigumula chinafika pa dziko lonse la pansi.
11-Pa 17, mwezi wachiŵiri, Nowa ali wa zaka 600, akasupe onse a madzi ambiri okhala pansi pa dziko anatumphuka, ndipo ku thambo kunatsekukanso, kuti madzi akhuthuke.

-Nowa ndi banja lake analowa m'chombo kupitira pa khomo limodzi lokha.

-Nyama zonse zinalowa m'chombo kupitira pa khomo limodzi lokha.

-Ili linali khomo limodzi lokha lopulumukira.
-Ili linali khomo limodzi lokha lothaŵila chilango.

-Kodi Mulungu anamupulumutsa Nowa chifukwa chakuti Nowa anali wabwino?
-Iyayi.

-Mulungu anamupulumutsa Nowa chifukwa chakuti amkakhulupilira kuti wachimwa.

-Mulungu anamupulumutsa Nowa chifukwa chakuti amkakhulupilira kuti tchimo lake limayenera kulandira chilango cha imfa yosatha.

-Mulungu anamupulumutsa Nowa chifukwa chakuti amkakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kumupulumutsa iye.

-Mulungu anamupulumutsa Nowa chifukwa chakuti amkakhulupilira mu lonjezo la Mulungu lotumiza Mpulumutsi.

-Kodi chinachitika ndi chiyani Nowa ndi banja lake pamodzi ndi nyama zonse zitalowa m'chombo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 7:16b

16-Kenako AMBUYE anatseka khomo la chombo.

-Nowa ndi banja lake pamodzi ndi nyama zonse zitalowa m'chombo, Mulungu anatseka chitseko.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anatseka chitseko?

-Kuti anthu amene anali mkati atetezedwe.
-Kuti anthu amene anali kunja kwa chombocho asathe kulowa, koma afe.

-Kodi anthu amene anali kunja kwa chombocho anakalira, Nowa anakatha kutsekula chitsekocho?

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti amene anatseka chitseko ndi Mulungu.

-Pamene Mulungu anamutulutsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni, kodi iwo anatha kubwereranso m'mundamo?
-Iyayi.



-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵatsekera kunja kwa mundawo poyika mngelo ndi lupanga la moto pa chipata chopitira ku mundako.

-Kodi pali amene angathe kuthaŵa ku chilango cha Mulungu?
-Palibe.
-Mulungu akaganiza zopereka chilango kwa anthu, palibe amene angachithawe chilangocho.

-Mulungu atatha kutseka chitseko cha chombocho, Iye anatumiza mvura.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 7:17-20

17-Chigumula chinagundika masiku makumi anayi pa dziko la pansi. Madzi anayamba kukwera pa dziko la pansi, ndipo chombo chinayamba kuyandama.
18-Madziwo anamka nakwelerakwelerabe, mpaka chombocho chidayandama pa madzi.
19-Kukwera kwa madzi kunapitilirabe mpaka kumiza msonga za mapiri atali atali kwambiri.
20-Tsono anakwelerakwelerabe mpaka kubzola msonga za mapiriwo ndi mamita asano ndi aŵiri.

-Kodi Mulungu anachipangitsa bwanji kuti chigumula cha madzi chikhale pa dziko lonse la pansi?

-Pachiyambi, Mulungu anaŵalekanitsa madzi.
-Mulungu anaŵasiya madzi ena pa dziko la pasi ndipo madzi ena anaŵayika kumwamba.